

Shire Valley Transformation Programme - 1 (SVTP-1)

Uthenga wa Ulimi wa Chitukuko ndi Kuchita Ulimi
ngati Bizinezi



Mbiri ya Pulojekiti ya SVTP

Boma la Malawi kudzera mu Unduna wa Zaulimi ndi thandizo lochokera ku World Bank, African Development Bank ndi Global Environmental Facility (GEF) likuyendetsa polojekiti ya Shire Valley Transformation Programme (SVTP). SVTP ndi polojekiti ya zaka khumi ndi zinayi imene ichitike m'magawo atatu motsagana.

Polojekiti ya SVTP idzakwanitsa kuthilira madzi mahekitala 43,370 kuchokera mu mtsinje wa Shire potenga madzi pa Kapichila damu kupita nawo maboma a Chikwawa ndi Nsanje kudzera mu ngalande. Izi zidzathandiza kuti madzi a ulimi wanthilira adzipezeka chaka chonse mmabomawa. Pulojekiti ya SVTP imatsatira ndondomeko izi:

- ✓ Kupindulira eni malo, kuwathandiza mu ulimi wa makono; Alimi omwe akufuna kutengapo mbali akuyenera kukhala m'magulu ndi kulima minda yawo pamodzi; kulola abizinezi apadela kupanga mgwirizano ndi eni malo;
- ✓ Kupereka mwayi kwa anthu a m'dera kusankha kukhala mamembala a sikimu;
- ✓ Kulipiritsa madzi kuti ndalama zake ziyendetsera ma sikimu. Izi zidzathandiza kuti ntchito za sikimu zidzakhale zopambana komanso zidzapitilire mpaka muyaya.

Cholinga cha chitukuko cha SVTP ndi kuchulukitsa zokolola ndi kupezeka kwa misika ku mabanja okhudzidwa ku chigwa cha Mtsinje wa Shire ndi kuthandiza kasamalidwe ndi kagwiritsidwe ka bwino ka zinthu za chilengedwe.

Zolinga za gawo loyamba la chitukukochi (2018 mpaka 2023) ndi:

- ✓ Kupereka mwayi wa ulimi wa nthirira wodalarika ndi ngalande zotayira madzi;
- ✓ Kupereka chitetezo cha malo kwa alimi ang'onoang'ono;
- ✓ Kulimbikitsa kusamalira malo otetezedwa kuchigwa cha Mtsinje wa Shire.

Cholinga Chachikulu cha Uthengawu

Cholinga cha uthengawu ndi kudziwitsa ndi kuthandiza kumvetsetsa momwe SVTP idzayendetsera chitukuko cha malimidwe ndi malonda a ulimi kwa alimi ang'ono ang'ono aku chigwa cha mtsinje wa Shire. Kufotokoza mwa tsatanetsatane za ubwino opangira ulimi pamodzi ndi kukhala m'magulu (mabungwe) a zamalonda, kusankha ndondomeko yomwe angachitire ulimi wawo, kusankha mtundu wa mbewu kapena ziweto zomwe akufuna kuchita malonda, kudziwa

njira zimene angatsatire kuti apeze chithandizo cha ndalama cha malonda awo kuchokera ku polojekiti, ndi momwe angapangire migwirizano ya malonda ndi mabungwe osiyanasiyana.

Gulu Lokhudzidwa

- ✓ Uthengawu kwambili ukupita kwa alimi ang'onoang'ono a polojekiti ya SVTP amene agwirizana zochita ulimi pamodzi kudzera m'mabungwe ngati ma Koparetivi, Asosiyeshoni kapena asosiyeshoni yoyanganira kagawidwe ndi kasamalidwe ka madzi (Water User Association- WUA);
- ✓ Uthengawu uthandizanso makomiti a mndondomeko ya kayendetsedwe ka ulangizi wa malimidwe m'mabomawa monga bungwe la alangizi loyanganira ntchito zaulimi pa boma (District Agriculture Extension Coordination Committee-DAECC), loyanganira ntchito za ulimi pa EPA (Area Stakeholder Panel- ASP), loyang'anira ntchito za ulimi pa boma (District Stakeholder Panel -DSP) komanso makomiti oyang'anira ntchito za malimidwe pa gulupu (Village Agriculture Committee -VAC) m'maboma a Chikwawa ndi Nsanje;
- ✓ Magulu ena omwe apindule ndi monga a zamalonda, ogulitsa malonda kunjira, alangizi a zaulimi, owona zachuma ndi amene amapereka malangizo osiyanasiyana pankhani zamalimidwe ndi malonda.

Dongosolo la Malo

- ✓ Pulojekiti ya SVTP kudzera mu Unduna Wowona za Malo, Nyumba ndi Chitukuko cha M'matauni idzathandizira kalemba ndi kutsimikizira mabanja omwe ali ndi malo amene adzafikiridwe ndi chitukukochi. Alimi ayenera kutsimikiziridwa kuti adzakhale eni ake a malo ngakhale atasankha ndondomeko zosiyanasiyana zoyendetsera mabungwe awo;
- ✓ Minda idzasonkhanitsidwa ngati bungwe limodzi la alimi pafupifupi mahekitala 500 kuti alimi azichita malonda pagulu;
- ✓ Minda yomwe idzakhale pamodzi idzayendetseredwa ndi bungwe la alimi lomwe lidzakhale litalembetsedwa ndi kuvomezedwa ndi boma;
- ✓ Minda idzalembetsedwa potsatira malamulo oyenera amene boma lakhazikitsa.

NJIRA/NDONDOMEKO ZA BIZINEZI ZOMWE ZIDZATSATIDWE

Alimi adzakhala m'magulu a makopaletivi, asosiyeshoni kapena makampani. Magulu a alimi adzasankha njira/ndondomeko yomwe adzatsate pa njira zinayi zomwe zamasuliridwa m'munsimu:

NJILA/NDONDOMEKO YOYAMBA- KUYENDETSEDWA NDI A KATSWILI A ULIMI WA BIZINEZI (AGRIBUSINESS MANAGERS)

- ✓ Alimi amapereka mpamba wawo wa bizinezi kudzera ku malo awo ndi kuthandiza kugwira ntchito;
- ✓ Kopaletivi imalemba katswili, akatswili kapena kampani yoyendetsa ulimi wabizinezi. Ntchito zonse zolima m'mundamu kuphatikiza kagawidwe ndi kasamalidwe ka madzi zimayendetsedwa ndi akatswiriwa. Chitsanzo m'malawi muno ndi momwe Phata Kopaletivi ku chikwawa ikuyendetsedwera. Kopaletivi inalemba kampani ya AGRICANE kuti igwire ntchito imeneyi;
- ✓ Mamembala a kopaletivi amapatsidwa gawo lina laling'ono la malo lomwe a malimapo mbewu zakudya ngati ndiwo zamasamba, chimanga ndi zina zotero. Gawoli limasamalidwa ndi mlimi mwiniwakeyo;
- ✓ Alimi amatengako mbali pothandizila ntchito zapakampani;
- ✓ Alimi amagawana phindu pomaliza pachaka molingana ndi kukula kwa malo omwe iwo anapereka ku kopaletivi.

UBWINO WOLEMBA NTCHITO A KATSWILI A ULIMI WABIZINEZI (AGRIBUSINESS MANAGERS)	KUIPA KOLEMBA NTCHITO A KATSWILI A ULIMI WA BIZINEZI (AGRIBUSINESS MANAGERS)
<ul style="list-style-type: none"> ✓ Pamakhala ukadaulo wa kayendetsedwe ka bizinesi, kasamalidwe ka chuma, kasungidwe ka ntchito zochitika pa mundapo ndi kuyanganira ogwila nthito pamundapo; ✓ Alimi amapindula kuchokera ku bizinesi akamagwira nawo ntchito ngakhale akangokhala; ✓ Pamakhala kugawana masomphenya ndi zolinga za bizinezi; ✓ Phindu limaperekedwa kwa alimi kutengera ndi mulingo wa munda omwe mlimi adapereka. 	<ul style="list-style-type: none"> ✓ Pamafunika kuti kampani iziyang'aniridwa pafupipafupi; ✓ Chiganizo pakagwiritsidwire ntchito kamalo chimakhala chochepeleko; ✓ Pamafunika kuti alimi amvetsetse momwe bizinesi iziyendera kuopa kukaikilana.

NJILA/NDONDOMEKO YACHIWIRI- KUYENDETSEDWA NDI ALIMI ANG'ONOANG'ONO OMWE ALI ENI MALO (SMALL HOLDER AGRIBUSINESS)

- ✓ Magulu alimi amagawanso malo kwa eni ake alimi malingana ndi kukula kwa malo amene mlimi aliyense anasonkha;
- ✓ Apa anthu samapereka lendi koma amakhala ngati akulima malo awo omwe ndichiyembekezo chakuti ulimi wawo udzikula pang'ono pang'ono mpakana kumakolola zochuluka pamalopo. Koma alimi ena amene amalephera kutsata ndondomeko ya kalimidwe kamakono amatha kukhala ndi ufulu wosiya kulima popereka ufulu ku bungwe la alimi kuti lipangitse lendi kwa mlimi wina kapena kusintha umwini. Anthu okhao amene amakhala m'deralo ndiwomwe azidzalowedwa kubwereka ndi kusintha umwini wa munda;
- ✓ Bungwe la alimi ndi lomwe limayang'anira dongosolo logawa ndi kusintha umwini wa malo. Ndiponso bungwe la alimiri limakhazikitsa gulu lina loyanganira kagawidwe ndi kasamalidwe ka madzi (Water User Association- WUA). Mlimi aliyense amayenera kumakhomera msonkho wa madzi malingana ndi kukula kwa malo ake. Ndipo dongosololi limakonzedwa ndi gulu loyang'anira za madzi. Mtengo wa kalipiridwe ka madzi umavomelezedwa ndi msonkhano waukulu wa alimi onse pachaka. Ntchito ya msonkho wa madzi ndi kuthandiza ntchito zina za pa sikimu monga kukonzetsa ngalande za madzi zikawonongeka;
- ✓ Alimi amathandizira ntchito zina za pasikimu mwachitsanzo kusamalila ngalande malingana ndi mgwirizano omwe ulipo;

- ✓ Munthu yemwe wabwereketsa munda, phindu lake limakhala ndime yomwe walima mbewu ya chakudya komanso ndalama zobwereketsa pa mundawo;
- ✓ Mulimi aliyense amalima pamunda pake;
- ✓ Malonda a zokolola amachitika pa gulu kapena pa mulimi payekha.

CHIDZIWITSO: Masikimu ambili M'malawi muno amatsata njira imeneyi

UBWINO WA ULIMI WOYENDESEDWA NDI ALIMI ANG'ONOANG'ONO OMWE ALI ENI MALO (SMALL HOLDER AGRIBUSINESS)	KUIPA KWA ULIMI WOYENDESEDWA NDI ALIMI ANG'ONOANG'ONO OMWE ALI ENI MALO (SMALL HOLDER AGRIBUSINESS)
<ul style="list-style-type: none"> ✓ Alimi amakhala ndi mphamvu yoyang'anila malo awo; ✓ Amatha kuyambilanso kulima iye mwini wake ngati anabwereketsa kwa wina. 	<ul style="list-style-type: none"> ✓ Kusoweka kwa upangiri, ukadaulo ndi zinthu zomwe zingathandize kuyendetsa bizinezi; ✓ Zimavuta kukwaniritsa zofuna za ogula maka mu ubwino kapena kuchuluka kwa katundu; ✓ Ulimi wamakono umavuta munthu kupanga payekha; ✓ Phindu limagawidwa potengera kuchuluka kwa katundu amene wagulitsidwa.

NJIRA/NDONDOMEKO YA CHITATU: NJIRA YOBWELEKETA MALO KWA ALIMI ANG'ONOANG'ONO NDI MAKAMPANI (NJILA YA NANSANGANYA/KASAKANIZA- MIXED MODEL)

- ✓ Bungwe la alimi limakhala ngati lothandiza kubwereketsa malo ku mamembala, anthu omwe si mamembala ndi makampani aza ulimi kuti alime kumundako;
- ✓ Bungwe la alimi limayendetsa nkhani zokhudza malo ndi kupereka madzi othilira kuminda pokhazikitsa gulu loyang'anira madzi la WUA;
- ✓ Malo obweleketsa ku kampani: Eni ake a bungwe la alimi adzalandila phindu potengera malo omwe anaperekedwa ku makampani;
- ✓ Malo olima wekha: Phindu limatengera kuchuluka kwa katundu amene wagulitsidwa osati kukula kwa malo kokha.

UBWINO WA NJIRA/NDONDOMEKO YOBWEREKETA MALO KWA ALIMI ANG'ONOANG'ONO NDI MAKAMPANI (NJILA YA NANSANGANYA/KASAKANIZA- MIXED MODEL)	KUIPA KWA NJIRA/NDONDOMEKO YOBWEREKETA MALO KWA ALIMI ANG'ONOANG'ONO NDI MAKAMPANI (NJILA YA NANSANGANYA/KASAKANIZA- MIXED MODEL)
<ul style="list-style-type: none"> ✓ Pamakhala mwayi ogawana maluso chifukwa chakuti makampani amakhala ali mbali ina ya mundawo; ✓ Gulu la alimi limayang'anira kugawa malo, kupeza misika ya alimi olima pa okha ndi kuyang'anira bungwe loyang'anira za madzi la WUA; ✓ Limathandiza kulimbikitsa mpikisano pakati pa alimi makamaka alimi ena akayamba kupeza phindu lochuluka; ✓ Mukhoza kubwereketsa malo anu ku kampani ndi kumalandira phindu ngakhale musakugwira ntchito iliyonse kumunda; ✓ Alimi ali ndi ufulu wosankha kumalima pa okha kapena kupanga ulimi pansi pa kampani. 	<ul style="list-style-type: none"> ✓ Pamakhala kusiyana pa njira ya mthirira ndi mbewu zomwe zimalimidwa pakati pa alimi; ✓ Pamakhala povuta kutsatira njira ya mthilira yamakono ngati central Pivot; ✓ Kumakhala kovuta kukwaniritsa zofuna za ogula pa msika makamaka kwa olima paokha paokha; ✓ Zimatha kuyambitsa mikangano ya malo kutengera m'mene bungwe la alimi lingabwereketsere malowo; ✓ Bungwe la alimi limakhala ndi ntchito yambiri monga kuyang'anira malo, kuyendetsa za WUA ndi kupereka madzi ku mabuloko. ✓ Eni malo amene amabwereketsa malo cholowa chimakhala chocheperako. ✓ Kulima kumachitika ndi mlimi payekha payekha mopanda dongosolo. ✓ Kugulitsa zokolola kumachitika ndi gulu la alimi kapena mlimi payekha payekha.

NJIRA/NDONDOMEKO YACHINAYI- NJIRA YOCHITA BIZINEZI LIMODZI PAKATI PA KAMPANI NDI BUNGWE LA ALIMI (JOINT VENTURE (JV) ENTERPRISES)

- ✓ Bungwe la alimi limapanga m'gwirizano ndi kampani yomwe ikufuna katunduyo. Kampaniyi imakhala ndi udindo wosonkha nawo chuma cholimira ndi kusamalira kumunda ndi kudzagwagula alimi katunduyo. Mwachitsanzo, mgwirizano pakati pa KAMA Kopaletivi ndi kampane ya Presscane. Alimi a KAMA adapanga m'gwilizano ndi kampani ya PressCane kuti alimi azilima mzimbe zogulitsa ku PressCane ndipo Press Cane iziwathandiza zipangizo za ulimi, chisamaliro ndi kudzagwagula alimiwo pa mtengo wogwirizana;
- ✓ Mabungwe a alimi amakhala ndi malo ndipo kampani imapereka thandizo la ndalama zoyendetsera ntchito zonse za pamundapo. Nthawi zina kampani pamodzi ndi gulu la alimi amagwirizana kukakongola ndalama kapena kupempha chithandizo cha ndalama ku mabungwe ena. Akakongola ndalama onse amabweza ngongoleyo;
- ✓ Eni ake a bungwe la alimi amalandira phindu kutengera kukula kwa malo awo;
- ✓ Eni ake alimi amakhalanso ndi gawo lina laling'ono lomwe amalima mbewu zakudya ndipo amasamala okha.

UBWINO WA NJIRA YOCHITA BIZINEZI LIMODZI PAKATI PA KAMPANI NDI BUNGWE LA ALIMI (JOINT VENTURE (JV) ENTERPRISES)	KUIPA KWA NJIRA YOCHITA BIZINEZI LIMODZI PAKATI PA KAMPANI NDI BUNGWE LA ALIMI (JOINT VENTURE (JV) ENTERPRISES)
<ul style="list-style-type: none"> ✓ Alimi samakhala ndi ntchito yayikulu yoyang'anira mbewu zomwe adasakha; ✓ Alimi amakhala ndi mwayi olupiridwa pa ntchito yomwe agwira; ✓ Zokolola zimachulukira pa munda chifukwa cha kasamalidwe kabwino ka mbewu; ✓ Zipangizo za ulimi zimakhala zopezekeratu kuchokera ku kampani; ✓ Misika imakhala iripo kale pa mbewu zomwe zalimidwa. 	<ul style="list-style-type: none"> ✓ Kusakhulupilirana pa zaphindu lomwe alimi ayenera kulandira; ✓ M'gwirizano umatha kuyipira mbali imodzi; ✓ Ndiposavuta anthu amaudindo kuwadyera anthu masuku pamutu; ✓ Andale akhoza kulowererapo; ✓ Kunenerera malonda kumakhala kovuta nthawi zina; ✓ Ndichapafupi kudiyeredwa masuku pa mutu chifukwa chakuti kampani ndi imene imapanga mitengo.

KUSANKHA NJILA YA BIZINEZI NDI KALANDIRIDWE KA CHITHANDIZO

- ✓ Alimi ali ndi mwayi osankha mtundu wa bizinesi omwe angapange kuyambira ku ziweto, mbewu, ulimi wa nsomba ndi zina zotero;
- ✓ Alimi akulimbikitsidwa kuyamba kudzalima mbewu izi: thonje, soya, nandolo, chimanga, nyemba, mpaka patapezekanso misika yina ya mbewu za mtengo wapatali komanso zomwe sizichedwa kuola monga mango, nthochi ndi tomato. Azidzalimbikitsidwa kumapanga ulimi wophatikiza mbewu ndi ziweto komanso ulimi wa nsomba mwazina;
- ✓ Mabungwe a alimi adzaphunzitsidwa kalembedwe ka bizinesi pulani kuti azidzalembe mabizinesi pulani malingana ndi bizinesi yomwe asankha. Ma bizinesi pulani azidzaunikidwa ndi akadaulo pakutha pa miyezi itatu iliyonse;
- ✓ Padzasankhidwa njira yokhazikika yosankhila momwe chithandizo chizidzaperekedwera. Izi zidzidzaunika kuthekera kwa kagwiridwe ka ntchito ndi ndalama, luso lakayendetsedwe ka kampani, kupezeka kwa zipangizo zaulimi pa msika ndi kupezeka kwa upangiri osiyana siyana;
- ✓ Chithandizo cha ndalama zothandizira mabungwe la alimi pa bizinesi yawo akalembe ndondomeko ya bizinesi (bizinesi pulani) chidzaperekedwa pamulingo umene walembedwa kuseliku.

NDONDOMEKO YOPEREKERA CHITHANDIZO CHA NDALAMA KUCHOKERA KU POLOJEKITI

GAWO LA CHITHANDIZO	NJIRA YA ULIMI				ALIMI AMENE
	1	2	3	4	AKULIMA KALE M'MAGULU
	Mlingo wachithandizo Kuchokera ku Polojekiti				
Kumanga ngalande zazikulu zobweretsa madzi ku buloko	100%	100%	100%	100%	Nzokambirana
Kumanga ngalande zothilira m'munda, zotaya madzi ndi misewu	90%	90%	90%	90%	0%
Kumanga zinthu zokhazikika monga maafesi, mosungila katundu ndi mafakitale	70%	70%	70%	0%	0%
Kugula zipangizo zoyendayenda monga magalimoto onyamula katundu ndi matractor olimila	50%	50%	50%	0%	0%
Ndalama zolipilira ntchito zothandizira kuti bizinezi iyende monga lendi, misonkho, magetsi, malipiro a anthu antchito	50%	50%	0%	0%	0%
Ndalama zomwe zimagwira ntchito zothandizira kugula zipangizo zomwe zimatheratu pompo mukazigwiritsa ntchito monga: mankhwala, mbewu ndi feteleza.	50%	50%	0%	0%	0%

MGWILIZANO WA MAGULU OSIYANASIYANA POGWIRA NTCHITO ZOSIYANASIYANA ZA MALONDA

- ✓ Pulojekitiyi idzalimbikitsa ndondomeko yabwino ya mgwirizano wa pakati pa mabungwe a alimi, boma ndi makampani ena ndi cholinga cholima ndi kugulitsa zokolola zapamwamba mogwirizana;
- ✓ Kudzakhhalanso ndondomeko yabwino yokumana ndi kukambirana kupititsa patsogolo maubale a malonda a magulu osiyanasiyana monga: alimi, ogulitsa zipangizo za ulimi, ogula zokolola, am'makampani, onyamula zokolola, opereka chithandizo cha ndalama kapena ngongole, magulu a alangizi, komanso amabungwe amene si a boma mukupereka upangiri wabwino;
- ✓ Mabungwe woyimira alimi pazosowa zawo (Farmers Unions) adzakhazikitsidwa ku masikimu aku chigwa cha Mtsinje wa Shire. Ndipo nthumwi zochokera ku sikimu iliyonse zidasankhidwa ndi kupanga m'gwirizano waukulu umodzi ku chigwa cha Mtsinje wa Shire. Gulu la ku chigwali lizidatumiza nthumwi zawo ku mabungwe akulu woyimira alimi M'malawi muno monga Farmers Union of Malawi (FUM) ndi ena amene angathandize alimi. Bungweli lidzakhala lothandizira kufikitsa madandaulo alimi ku boma;
- ✓ Pulojekitiyi idzalimbikitsa ndikukhazikitsa malo otchuka ndi ulimi umodzi aku dela. Pulojekitiyi idzathandizanso aku Unduna wa Zamafakitale, Malonda ndi zokopa alendo ndi a Malawi Investment and Trade Centre (MITC) kuonetsetsa kuti pakhazikitsidwa malo abwino wolimira pamodzi mkatikati mwa malo a pulojekiti ndi kuwunikanso malamulo okhudzana ndi kagawidwe ka malowa;
- ✓ Ntchito yokhazikitsa malo opanga ulimi umodziwu idzathandiza kulinganitsa mabungwe amene si a boma kumabizinezi m'derali makamaka pokhazikitsa mafakitale ndi malo okopa alendo;
- ✓ Pulojekitiyi idzathandizira mabungwe osiyanasiyana kupeza mwayi wa ndalama zopangira mabizinezi monga ngongole, kuthandizidwa mwaulere (challenge funds) ndi ndondomeko yosungila katundu wa alimi ku malo osungira (warehouse). Njira ya kusunga katundu wa alimi podikira kupeza msika wabwino imathandiza kuti alimi apeze ndalama zina ku banki asanagulitse katundu wawo ndipo banki limadzatenga ndalama zake alimi akapeza msika pa mtengo wabwino;
- ✓ Pulojekiti idzalumikizitsa alimi, ogulitsa, okonza zokolola, misika yopezeka ndi ena onse okhudzidwa ndi bungwe la alimi ndi kusaka njira zina zatsopano kuonjezerapo njira ya malonda opikisana.

KUONJEZERA UKADAULO

Polojekitiyi idzapereka malangizo, maphunziro komanso upangiri pankhani za ulimi, kayendetsedwe ka ulimi wamthirira, misika yapamwamba, kayendetsedwe ka bizinezi, kagwiritsidwe kabwino kamalo ndiponso upangiri wina uliwonse molingana ndi kafukufuku amene adzachitike pounika zosowa za alimi.

ZOTSATIRA NDI ZOYEMBEKEZERA

Pakhomo la munthu

- ✓ Kukhala ndi chakudya chokwanira;
- ✓ Kuchuluka kwa chuma chifukwa chokolola katundu wochuluka, wapamwamba ndi kugulitsa pa mtengo wabwino;
- ✓ Kukhala ndi chakudya cha magulu onse chopatsa nthanzi.

Pamudzi/ M'dera

- ✓ Kusinthika kwa miyoyo ya anthu kudzera mu ulimi opindulitsa;
- ✓ Chakudya chokwanira komanso chopatsa thanzi kudzela mukupezeka kwa chuma chokwanira;
- ✓ Chitukuko cha mdera ndi malo ena ozungulira chimakula kudzela muntchito zachitukuko monga kumangidwa kwa misewu ndi magolosale.

M'dziko

- ✓ Kuchuluka kwa ndalama zakunja;
- ✓ Kupezeka kwa ntchito m'dziko;
- ✓ Kukhazikitsidwa kwa makampani/mafakitale a zaulimi;
- ✓ Kukhazikitsidwa kwa misika ya zaulimi.

Zithunzi:

1. Ulimi wothirira m'munda wa mzimbe ku Illovo mboma la Chikwawa
2. Alimi a chimanga pa Sikimu ya Nabomba, Mbewe EPA ku Chikwawa
3. Ulimi waziweto ku Famu ya Issa m'boma la Chikwawa

Kuti mumve zambiri, walengani pa intaneti pa www.svtp.gov.mw

Lembani kalata ku keyala iyi:

The Project Coordinator,
SVTP,
P/Bag 379,
Chichiri,
Blantyre 3
Phone: 01 828 709

Kapena lembani kalata yapa intaneti ku:

The Project Coordinator: projectcoordinator.doi@svtp.gov.mw
Communications: info.doi@svtp.gov.mw